Kodi Munthu Akafa Amapita Kuti? (Gawo 2)

Nkhaniyi yachokera m'mutu 6 wa buku lakuti, *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* lomwe likupezeka pa jw.org/ny.

CHOLINGA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso zifukwa zake, fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa, kenako ganizirani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.

KODI ZOTI ANTHU AZIFA NDI ZIMENE MULUNGU ANKAFUNA?

1 GANIZIRANI MOZAMA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

N'chifukwa chiyani anthu ena angayankhe kuti inde?

N'chifukwa chiyani anthu ena angayankhe kuti ayi?

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

Nanga n'chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

www.jw.org © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Anthu sanalengedwe kuti azifa.

(Werengani mutu 6 m'buku lakuti *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani*, ndime 9 mpaka 14.)

Werengani Genesis 2:16, 17.

Kodi mavesi amene mwawerengawa akusonyeza kuti chifukwa chimene Adamu anafera n'chiti?

_____

_____

_____

Kodi Adamu akanamvera Mulungu, akanakhalabe ndi moyo mpaka lero?

_____

_____

_____

Dokotala wachikondi amauza anthu amene akudwala kuti azipewa zinthu zimene zingawononge thanzi lawo. Yehova nayenso anauza Adamu ndi Hava kuti apewe kuchita zinthu zimene zingawononge moyo wawo

www.jw.org © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Mlengi wathu wachikondi amafuna kuti atumiki ake akhale ndi moyo.

(Werengani mutu 6 m'buku lakuti *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani*, ndime 15 mpaka 20.)

Werengani 1 Yohane 4:8.

Kodi khalidwe lalikulu la Mulungu ndi liti?

Werengani Machitidwe 24:15; Chivumbulutso 4:11.

Kodi malembawa akusonyeza kuti Yehova ndi wotani?

Kodi kudziwa chifukwa chimene anthufe timafera kumakhudza bwanji m'mene inuyo mumaonera Yehova Mulungu?

www.jw.org © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

WINA AKANENA KUTI . . .

Mulungu anatiika padziko lapansi n'cholinga choti tiyesedwe kaye tisanapite kumwamba.

MUNGAYANKHE KUTI . . .

Anthu ambiri anganene kuti zimenezo n'zoona. Koma ine ndimakhulupirira zosiyana ndi zimenezo chifukwa . . .

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze bwanji vesilo pomuthandiza malinga ndi zimene amakhulupirirazo?

_____

WINA AKANENA KUTI . . .

Aliyense amafa; ndipo zimenezi sizachilendo chifukwa ndiwo mapeto a moyo.

MUNGAYANKHE KUTI . . .

N'zoona kuti panopo aliyense amafa. Koma ine sindimakhulupirira kuti Mulungu anasankhira dala kuti anthu azifa . . .

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze bwanji vesilo pomuthandiza malinga ndi zimene amakhulupirirazo?

_____

www.jw.org © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania